

NAME: _____ NO.: _____



NORTHERN EDUCATION DIVISION MOCK EXAMINATION

2026 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION

CHICHEWA

Subject number: M032/II

Wednesday, 25th March

Time allowed: 2hrs

1: 00 am- 3: 00 pm

PAPER II

(Malikisi 90)

Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba khumi ndi atatu.

2. Pepalali lili ndi magawo anayi: A,B,C ndi D. yankhani mafunso onse m'magawo onsewa.

3. Lembani nambala yamayeso pamwamba pa tsamba lililonse la pepalali.

4. Muchitebulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochomga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

Funso	Chongani funso ngati mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6			
7			
TOTA			
L			



NAME: _____ NO.: _____

GAWO A (Malikisi 40)

Malamulo a Chiyankhulo

Langizo: Yankhani mafunso onse m'gawo ili.

1. a. Kodi mayina awa adachokera ku chiyankhulo chanji?

(i) kachasu _____

(ii) thaulo _____

(iii) ndege _____

(iv) gomo _____

(Malikisi 4)

b. Kodi afotokozi ali m'munsiwa adapangidwa bwanji?

(i) wamkazi

(ii) zachitsulo

(iii) tofewa

(Malikisi 6)



NAME: _____ NO.: _____

2. a. Pangani ziganizo ndi nthawi za aneni zotsatirazi:

(i) nthawi yatsopano yopitirira

(ii) nthawi yakale yakawirikawiri

(iii) nthawi yamtsogolo yathayi

(Malikisi 6)

b. Tchulani mitundu ya agwirizanitsi omwe ali ndi mzere kungsi kwake mu ziganizo zotsatirazi

(i) Zala zotere zimasunga umve.

(ii) Abambowa afika kumene.

(iii) Amayi ako akukuyitana.



NAME: _____ NO.: _____

(iv) Pamudzi pano ndapakonda.

(Malikisi 4)

3.a. Lembani ziganizo zosonyeza ntchito za ‘ti’ zotsatirazi ndipo
mutseke mzere

kunsi kwake

(i) Kukhala tside lamneni

(ii) Kukhala mgwirizanitsi wamchitidwantchito

(iii) Kukhala mphatikiram’mbuyo wochepetsa

(Malikisi 6)

b. Tchulani ntchito za akapandamneni omwe atsekedwa mzere kunsi
kwawo mziganzo zotsatirazi.

i. Iye amakonda nyama yowotcha.

ii. Khazikani chakudyacho pa tebulo lalikulu.



NAME: _____ NO.: _____

iii. Mayo ine! Chipupa Chagwera mwana.

iv. Munthuyo adali wamtali zedi.

(Malikisi 4)

4. Phwanyani chiganizo chotsatirachi pounika mawu aliwonse
pawokhapawokha

Mariya wabwera dzulo.

(Malikisi 10)

Gawo B (Malikisi 20)

Kumvetsa nkhani ndi kusanthula chiyankhulo



5. Werengani nkhani yili munsiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse

Mudzi wina wotchedwa Sekwa udali waukulu koposa komanso udali mudzi wopanda phokoso. Udalinsu mudzi wosadziwa kulima ndipo njala chaka ndi chaka imavuta. Anthu ake, milandu nayo imawavuta kuweruza kwake kotero kuti ina imatha zaka zitatu isanaweruzidwe chifukwa chakugotomala kwa mfumu ndi nduna zake.

Mnyamata wina dzina lake Kachengwa adakwatira pamudzi pamenepa ndipo anthu ambiri poyamba amamukonda chifukwa choseketsaseketsa akamacheza ndi anthu. Analinsu ndi luso polongosola bwino nkhani ndipo anthu ambiri amati iyeyo ndi mkamwini wabwino. Mkazi wa Kachengwa anali Damalisi.

Tsiku lina Kachengwa anakhala nawo pa bwalo loweluzira milandu, koma adaona kuti mfumu pamodzi ndi abwalo ake adalibe luso loweluza milandu. Iye adayimirira nati: mlandu wa ndewu uja mukadatere, wolanda mkazi wa mwini mukadatere. Atatha kuyankhula adatuluka ndipo anthu ambiri anamutama chifukwa cha nzeru nzake zopambana. Koma mfumu ndi nduna zake sizidasangalale chifukwa zidachita manyazi pagulu. Anthu enanso adati, ‘komatu kali kukhosi umanena, Kachengwa uja sanapange bwino popeza wanyazitsa bwalo lathu’.

Pamene izi zimamveka, anthu ena anayamba kudana naye. Koma anali ndi luso lodziwa kulima. Iye adadzadza nkhekwe zambiri ndipo adayamba



kudzitamandira ndi kuti, ‘anthu okhala pamudzi pano, onse ndi zidzete, chipanda ine akadafa ndi njala. Pakhomo panga pano pali ana mbwee monga ana ankhumba kufuna ine ndiwadyetse. Azimayi atamva izi sizidawasangalatse ndipo iwo adayamba kunena nati, ‘kodi inu azimunanu pamudzi pano, mufuna Kachengwayu atilowe mchala?’

Kachengwayu tsiku lina adachita ndewu ndipo kubwalo kuja nkhaniyo sanavutike nayo chifukwa chochenjera pakamwa ngakhale adalakwa ndi iyeyo. Tsiku lina adapha munthu koma nkhaniyo itapita kubwalo sanatsutsidwe chifukwa chodziwa kuyankhula. Tsiku lina adatentha nyumba ya mdani wake ndipo mlandu udamkomera. Tsiku lina adagwaza ng’ombe ya mfumu ndi mpaliro chifukwa idakadya chimanga m’munda mwake ndipo nyama yake adadyanso yekha. Koma atapita naye kubwalo milandu yonse adalephera kumtsutsa chifukwa chodziwa kuyankhula.

Anthu onse pamudzipo adadana naye tsopano ndipo usiku wina adachita upo kuti amuchitire chiwembu kuti achimine. Ndipo Kachengwa ali ku mowa pa mudzi wina, mfumu idasonkhanitsa anthu kunyumba kwake. Mfumu idati, ‘anthuni, pamudzi pano Kachengwa atilowa ngati sitikhala maso. Ine ndakonza kuti ndiphe nkhoa yanga yonenepa ija. Tsono wina apite kwa mkazi wake akatenge malaya ake oyera aja kuti tidzaviike m’magazi a nkhosayo nkukabisa m’nyumba mwake. Pafunikanso kumuuza Damalisi kuti akangoulula adzaphedwa nthawi yomweyo. Tsono ine ndidzakuwa m’mawa kuti ‘Dzaoneni dzaoneni! Mukabwera ndidzaona mochitira mwake.



NAME: _____ NO.: _____

Izi zidachitikadi, ndipo m'mawa kutacha, mkuwo udamveka ndipo onse adapita kwa mfumu. Woyambirira kufika kwa amfumu adali Kachengwa amene. Mfumu idati, munthu wandiphera nkhoa yanga usiku. Tsono nonsenu musachoke ayi pakuti nditumiza anyamata anga achitetezo kuti akalowe m'nyumba zanu nakafunefune n'kupeza nyama yake.

Anyamata achitetezo aja adayamba kugubuduza m'nyumba zonse ndipo pofika m'nyumba ya Kachengwa adapezamo malaya ake oyera ali magari psuu! Komanso adapezamo mutu wa nkhoa. Pofika kwa mfumu anyamatawo adati, ife tapeza malaya a magari komanso mutu wa nkhoa kunyumba ya Kachengwa.

Mfumu nthawi yomweyo idafunsa nati, 'kodi malayawa mwiniwake ndi ndani? Iye adati mwini wake ndine. Mfumu idafunsanso, 'wapha nkhozayi ndi ndani? Kachengwa adayamba kunjenjemera popeza sadadziwe chimene chidachitika ndi malaya ake. Anthu onse adamukuwiza kuti, 'wakubayo! Watithera zinthu pamudzi pano uchoke!

Mfumu idalamula kuti abweze nkhoa khumi komanso achoke chifukwa sangakhale ndi tsizinantole. Kachengwa adatenga malaya ake nalunjika njira yakwawo dzuwa likuswa mtengo.

5. a. (i) Kodi Kachengwa adakwatira pamudzi uti?

(Malikisi 1)



NAME: _____ NO.: _____

- (ii) Tchulani mavuto **awiri** omwe Kachengwa adawapeza pamudzi pomwe adakwatira.

(Malikisi 2)

- (iii) Chifukwa chiyani poyamba anthu a m'mudzimo ankamukonda Kachengwa?

(Malikisi 2)

- (iv) N'chifukwa ninji Damalisi sadaulule chiwembu chomwe anthu adakonzera mwamuna wake?

(Malikisi 1)

- (v) N'chiyani chomwe Kachengwa adalakwitsa pamudzipo?

(Malikisi 2)

- (vi) Kodi anthu am'mudzimo adachita chiyani kuti athane ndi Kachengwa?



NAME: _____ NO.: _____

(Malikisi 2)

- (vii) Tsimikizani kuti Kachengwa adalakwitsa kudzudzula a mfumu ndi nduna zawo.

(Malikisi 2)

b. Kusanthula chiyankhulo

- (i) Perekani matanthauzo a mawu awa:

1. atilowa m'chala _____
2. achimine _____
3. zidzete _____
4. sitikhala maso _____

(Malikisi 4)

- (ii) Fotokozani mmene mikuluwiko yotsatirayi ikugwirizanirana ndi nkhani yomwe mwawerenga.

1. Apawo ndi mizu ya kachere ikumana pansu.

2. Pamudzi pakakhala pa zitsiru mkamwini asamakulirepo mwendo.



NAME: _____ NO.: _____

(Malikisi 4)

GAWO C: (Malikisi 15)

Chifupikitso

5. Werengani nkhaniyi mosamala ili ndi mawu 124 ndipo muyifupikitse kuti ikhale ndi mawu osachepera 43 ndipo osapitirira 48.

NDEVUZAMWAYI

Pali anthu ena omwe amaganiza kuti ndalama sizingapezeke popanda kuchitira mankhwala. M'modzi wa anthu oterewa adali bambo Ndevuzamwayi omwe adalemera mwa njira yamankhwala.

Pofuna kulemera iwo adapita kwa sing'anga yemwe adawauza kuti akaphe mwana wawo woyamba. Atabwerera kumudzi bambowa adaphadi mwanayo natengako zizimba zochitira mankhwala kuti alemere. Ndipo bambowo adalemeradi.

Posakhutisidwa ndi chuma chomwe adayamba kupeza, iye adapitanso kwa sing'angayo napatsidwa mankhwala obero ndalama omwe chizimba chake chidali bongo, chiwindi ndi mano a m'bale wawo. Kotero, bambowa adapha mchimwene wawo n'cholinga chotengako zizimba zochitira mankhwalawo.



NAME: _____ **NO.:** _____

Atachita mankhwalawo ndi zizimbazo, bambowa adanka mtsogolo pa chuma kotero adapeza ndalama zogulira zinthu monga galimoto zisanu ndi zigayo khumi. Zidali zomvetsa chisoni anthu atazindikira za mchitidwewu. Bambo Ndevuzamwayi adamangidwa kukhala kundende moyo wawo wonse ndipo chuma chonse chidatha.

This image shows a single sheet of white paper with horizontal ruling lines. The lines are evenly spaced and run across the width of the page. There are no margins, text, or other markings on the paper.

NAME: _____ NO.: _____

Gawo D (Malikisi 15)

Chimasuliro

Masulirani nkhani yotsatirayi m' Chichewa chomveka bwino

HAVING PEACE OF MIND

A peaceful life means beginning each day with personal satisfaction and happiness. Being at peace is considered by many to be a healthy condition. The peace of mind is generally associated with happiness. Positive thinking, combined with positive deeds, creates positive results.

On the other hand, negative thinking, combined with negative deeds, is a destructive force that leads to misery, pain and suffering. If someone does not have peace, the person may end up making deadly decisions. Malawian youth is encouraged to avoid heartbreak and stress to have life full of peace.

[illegible]

This image shows a blank sheet of white paper with horizontal ruling lines. The lines are evenly spaced and run across the width of the page. There are no margins, text, or other markings on the paper.

